-Mulungu anaŵatetezanso a Isirayeli chifukwa chakuti Iye ankafunanso kuti adzatumize Mawu AKE, Bayibulo, kwa anthu onse kupitira mwa Aburahamu ndi a Isirayeli.

-Tikakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu adzatipulumutsa ife.
-Ngati sitidzikhulupilira mwa Mulungu, Mulungu sadzatipulumutsa ife.



# PHUNZIRO LA 30

1. Ngakhale kuti Mulungu anatumiza milili yowopsa ngati imeneyi kwa Farawo ndi a Ejipito, kodi Farawo anaŵalola a Isirayeli kuti adzipita?
-Iyayi

2. Kodi mulili womaliza umene Mulungu anatumiza unali otani?
-Mulili womaliza umene Mulungu anatumiza unali wakupha ana onse amuna oyamba kubadwa a a Ejipito ndi nyama zomwe.

3. Ngati a Isirayeli ankafuna kuti apulumutsidwe ku imfa, kodi ankayenera kutsatira chiyani mosamalira?
-Ankayenera kutsatira malamulo amene analamula Mulungu.

4. Kodi Mulungu anaŵalamula kuti achite chiyani a Isirayeli kuti ana awo achisamba asamwalile?
-Anaŵalamula kuti asankhe mwana wa nkhosa kapena mbuzi wa mphongo wa chaka chimodzi ndipo opanda chilema.
-Anaŵalamula kuti aphe mwana wa nkhosa kapena wa mbuzi wa chaka chimodzi wa mphongo, wopanda chilema, ndikutsira magazi ake m'mbale.
-Anaŵalamula kuti atenge magazi a nyamayo ndi kuwaza pa mphuthu ziŵiri za chitsekozo, ndi pamwamba pa chitseko cha nyumba imene akadyeremo nyamayo usiku umenewo.
-Anaŵalamula kuti akhale mkati mwa nyumba imene inali ndi magazi pa chitseko chake mpaka m'maŵa.
-Anaŵalamula kuti asaphwanya fupa lina lililonse la mwana wa nkhosa kapena mbuzi.

5.A Isirayeli anakapanda kuchita zonse ngati m'mene Mulungu anaŵalamulilila, kodi chinakaŵachitikira chiyani?
-Muliliwo unakafika kwa iwowo, ndipo ana awo amuna achisamba anakamwaliranso.

6. Kodi Mulungu adzaŵalora anthu kuti adzipulumutse okha mu njira zawo?
-Iyayi.

7. Kodi ndi njira ya ndani yokhayo imene idzatipulumutse ife?
-Njira ya Mulungu.

8-A Isirayeli akadzaŵamvera malamulo a Mulungu, kodi Mulungu analonjeza kuti adzachita chiyani?
-Mulungu ananalonjeza kuti mulili omalizawo siwudzafika kwa iwowo, ndipo ana awo achisamba amuna sadzamwalira.

9. Kodi Mulungu anaŵapha ana achisamba onse a a Ejipito ngati m’mene ananenera?
-Inde.

10. Kodi panali mwana wa chisamba aliyense wa a Isirayeli amene anaphedwa?
-Panalibe.

11. Kodi chifukwa chiyani panalibe mwana wa chisamba wina aliyense wa a Isirayeli amene anaphedwa?
-Chifukwa chakuti a Isirayeli anamumvera Mulungu ndipo anapaka magazi pamwamba pa chitseko ndi pa mphuthu ziŵiri za chitsekocho.

12. Chifukwa chakuti a Isirayeli anamumvera Mulungu, kodi Mulungu anasunga lonjezo lake ndipo anazipitilira nyumba za a Isirayeli.
-Inde.

13. Kodi Mulungu amachita zimene walankhula nthaŵI zonse?
-Inde.

14. Mwana wa chisamba wa Farawo ndi a Ejipito onse at-



-Mulungu anamumiza Farawo pamodzi ndi asilikali ake mnyanja yofiira ija.
-Panalibe msilikali wina aliyense amene anapulumuka.

-Kodi Farawo anakatha kulimbana ndi Mulungu ndikumupambana IYE?
-Iyayi.

-Kodi ndi ndani amene angalimbane ndi Mulungu ndikumupambana IYE?
-Palibe.

-Kodi panali mu Isilayeli wina aliyense amene anafa?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:29-30

29-Koma a Isirayeli onse aja adawoloka nyanjayo pansi pali powuma, madzi atangayima pa mbali zonse ziŵiri.
30-Pa tsiku limenelo, AMBUYE, adaŵapulumutsa a Isirayeli kwa a Ejipito. A Isirayeli adaŵawona a Ejipito ali ngundangunda m’mbali mwa nyanja.

-Panalibe mu Isirayeli wina aliyense amene anafa.

-Kodi chifukwa chiyani panalibe mu Isirayeli wina aliyense amene anafa?
-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵateteza iwowo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵateteza a Isirayeli kuti asafe?

-A Isirayeli anali zidzukulu za Aburahamu.

-Mulungu anaŵateteza a Isirayeli chifukwa chakuti IYE analonjeza zotumiza Mpulumutsi kupitira mwa Aburahamu, ndi a Isirayeli.

imene kunali  Farawo pamodzi ndi asilikali ake, iwowo ankapitilizabe kuŵatsatira a Isirayeli.

-Farawo pamodzi ndi asilikali ake ankaŵatsatirabe a Isirayeli mpaka Mnyanja yofiira.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:23

23-A Ejipito aja adaŵalondora a Isirayeliwo mpaka kukaloŵa nawo m'nyanja muja. Akavalo onse a Farawo adaloŵa m'nyanja, pamodzi ndi magaleta ake ndi oŵayendetsa ake omwe.

-Kodi Mulungu anachita chiyani, Farawo pamodzi ndi asilikali ake ataŵatsatira a Isirayeli mpaka Mnyanja yofiira ija?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:24-28

24-Tsono kusanache m'maŵa ndithu, AMBUYE, ali mchipilala cha mtambo ndi moto, adayang'ana a nkhondo  a a Isirayeli ndipo adaŵachititsa mantha.
25-Adapinda mikombero ya magaleta awo, kotero kuti magaletawo ankayenda movutika. Pamenepo a Ejipito aja adati, "Tiyeni tiŵathaŵe a Isirayeliŵa, chifukwa chakuti AMBUYE akuŵamenyera nkhondo, kulimbana nafe."
26-Apo AMBUYE adamuwuza Mose kuti, "Tambalitsa dzanja lako ku nyanjako kuti madziwo abwerere, ndi kuwamiza a Ejipitowo pamodzi ndi magaleta awo ndi oŵayendetsa ake omwe."
27-Chomcho Mose adatambalitsa dzanja lake ku nyanja, ndipo m'mene kunkacha, nkuti madziwo akubwerera m'malo mwake. A Ejipitowo adayesa kuthaŵa, koma AMBUYE adaŵabwezera m'nyanja momwemo.
28-Ndipo madziwo adabwerera, namiza magaleta aja ndi oŵayendetsawo, pamodzi ndi gulu lonse la nkhondo la Farawo lija linkaŵatsatirali. Palibe ndi m'modzi yemwe amene adapulumuka.



amwalira, kodi Farawo anachita chiyani?
-Farawo anaŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

15. Kodi Farawo angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Iyayi.

16. Kodi pali amene angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Palibe.

-Mulungu anaŵapulumutsa a Isirayeli ku mavuto a ukapolo ndi Farawo, ndipo anaŵatsogolera a Isireyeli putuluka mu Ejipito.

-Kodi Mulungu ankaŵatsogolera a Ejipito kupita ku dziko lanji?
-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli kubwelera ku dziko la kanani.

-Kanani linali dziko limene mulungu anamulonjeza Aburahamu, Isaki ndi Yakobo, ndi zidzukulu zawo.

-Pamene a Isirayeli ankapita ku Ejipito anali akwana 70 okha basi.

-Tsopano atakhala mu Ejipito kwa zaka zokwana 400, a Isirayeli ankakwana 2 miliyono.

-Kodi Mulungu anakatha bwanji kuŵatsogolera a Isirayeli 2 miliyoni?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 13:21-22

21-NthaŵI ya masana AMBUYE ankaŵatsogolera ndi chipilala cha mtambo namaŵalangiza njira. Ndipo mu nthaŵI ya usiku , ankaŵatsogolera ndi chipilala cha moto, kuŵawunikira njira kuti adziyenda masana ndi usiku womwe.

22-NthaŵI zonse chipilala cha mtambo chinkaŵatsogolera anthu masana, ndipo chipilala cha moto chinkaŵatsogolera usiku.

-Kodi Mulungu ankaŵatsogolera bwanji a Isirayeli 2 miliyoni?

-Masana, Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli ndi mtambo.

-Usiku, Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli ndi chipilara cha moto.

-Kodi Mulungu anakakhala kuti sakuŵatsogolera a Isirayeli, anakakudziŵa kumene ankapita?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anakakhala kuti sakuŵatsogolera a Isirayeli, chinakaŵachitikira ndi chiyani?
-Anakasokera ndikufa.

-Chifukwa chakuti Mulungu ankaŵakonda a Isirayeli, ankaŵatsogolera iwowo kuti asasokere ndikufa.

-Mulungu anaŵatsogolera a Isirayeli mpaka ku nyanja yotchedwa Nyanja yifiira.

-Atafika ku Nyanja yofiira, Mulungu anaŵawuza a Isirayeli kuti apume kwa kanthaŵi.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:1-3

1-Tsopano AMBUYE anamulamula Mose kuti,
2-"Uŵawuze a Isirayeli kuti, abwerere, amange zithando patsogolo pa Pihahiloti pakati pa Migidoli ndi nyanja , moyang'anana  ndi Baala- Zefoni. Mumange zithando pamenepo m'mbali mwa nyanja.
3-Apo Farawo adzaganiza kuti, "A Isirayeli asokonezeka, akungoyendayenda m'dzikomo, azingidwa ndi chipululu."



-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani kunali kosavuta kwa Mulungu kutsagula Nyanja yofiira?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anayilenga Nyanja yifiirayo.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyang'anira Nyanja zonse.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wa mphamvu kwambiri, ndipo akhoza kuchita china chilichonse.

-A Isirayeli anayamba kuwoloka Nyanja yofiira ija.

-Chifukwa chakuti Farawo ndi asilikali ake ankabwera kudzaŵagwiranso a Isirayeli, kodi Mulungu anachita chiyani pofuna kuŵapulumutsa a Isirayeli?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:19-20

19-Apo mngelo wa Mulungu, yemwe ankaŵatsogolera a Isirayeli aja, adakakhala chakumbuyo kwawo. Mtambo womwe unkakhala patsogolo pawo uja, udakakhalanso chakumbuyo kwawo.
20-Unali pakati pa gulu la nkhondo la a Ejipito ndi gulu lankhondo la a Isirayeli. Chomcho panali mtambo ndi mdima, kotero kuti magulu a nkhondo aŵiriwo sadayandikane usiku onse.

-Mulungu anayika mtambo pakati pa a Isirayeli ndi Farawo pamodzi ndi asilikali ake.

-Mtambowo akuwala ku mbali imene a Isirayeli anali ndipo unkapangitsa mdima ku mbali imene Farawo pamodzi ndi asilikali ake anali.

-Ngakhale kuti mtambowo unkapangitsa mdima ku mbali

-Mulungu yekha ndi amene anatha kupanga njira yoŵapu-
lumutsira iwowo.

-Manja ndi miyendo ya Isaki itamangidwa, ndipo mpeni wa Aburahamu unayamba kumupereke iye ngati msenmbe, Isaki sanakatha kudzipulumutsa yekha.

-Mulungu yekha ndi amene anakatha kupanga njira yomupulumutsira Isaki.

-Tsopano a Isirayeli anakodwa, sanakathanso kudzipulumutsa okha.

-Mulungu yekha ndi amene anakatha kupanga njira yoŵapulumutsira a Isirayeli.

-Ngati m'meme analili Mulungu kupanga njira yoŵapulumutsira a Isirayeli, Mulungu yekhanso ndi amene angathe kukupulumutsani inu.

-Kodi Mulungu anapanga njira yoŵapulumutsira a Isirayeli?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:21-22

21-Tsopano Mose adatambasula dzanja lake pa nyan-
ja, ndipo pompo AMBUYE adayiwumitsa nyanja ija, pog-
wiritsa ntchito mphepo ya mkunthoya ku vuma, imene
idawomba usiku onse ndi kuwumitsa nyanjayo. Madziwo
adagaŵikana,
22-ndipo adakhala ngati chipupa pa mbali zonse
ziŵiri, chomcho a Isirayeli adawoloka powuma.

-Mulungu anayilamula Nyanja yofiira kuti itsaguke ndipo ipange njira yakuti a Isirayeli awoloke mowuma.

-Kodi kunali kovuta kwa Mulungu kutsagula Nyanja yofiira?



-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵatsogolera a Isirayeli mpaka m'mbali mwa Nyanja yofiira?

-Mulungu ankafuna kuti aŵawonetse a Isirayeli ndi a Ejipito kuti IYE ndi Mulungu m'modzi yekha.

-Kodi amene anamuwuza Mulungu zimene Farawo adziganiza ndani?
-Palibe.

-Kodi Mulungu anadziŵa bwanji zimene Farawo adzaganize?

-Mulungu ankalidziŵa ganizo lililonse la Farawo, Farawoyo asanayambe kuganiza.

-Mulungu amaŵadziŵa maganizo athu onse ife tisanayambe kuŵaganiza.

-Tiyeni timve zimene Farawo ankanena:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:5-9

5-Mfumu ya ku Ejipito atamva kuti anthu athaŵa,
Farawo, mfumu ya ku Ejipito, pamodzi ndi nduna zake
zonse , adasintha maganizo pa za a Isirayeliwo ndipo adati,
"Kodi ife tachita chiyani pamenepa? Talola a Isirayeli kuti
athaŵe ndi kuleka kutitumikira!"
6-Pamenepo Farawo adakonzetsa galeta lake la
nkhondo , ndipo adawuza asilikali ake kuti apite naye
limodzi.
7-Adatenga magaleta a mphamvu 600 pamodzi ndi
magaleta ena onse ndipo adayika atsogoleri pa magaleta
onsewo.
8-AMBUYE adamuwumitsa mtima Farawo, mfumu ya
ku Ejipito, ndipo iye adaŵalondola a Isirayeli, amene

ankachoka monyada.

9-A Ejipito, akavalo ndi magaleta onse a Farawo, oy-endetsa magaletawo, okwera pa makavalo ndi gulu la nkhondo la Farawo, adaŵalondola a Isirayeli aja nakaŵape-za pa malo pomwe adamanga zithando paja, pafupi ndi Pihahiroti, moyang'anana ndi Baala-Zefoni.

-Farawo ankaganiza zowagwiranso a Isirayeli.

-Chomcho , Farawo anasonkhanitsa asilikali ake, ndipo anapita kuti akaŵagwirenso a Isirayeli.

-Kodi amene ankamutsogolera Farawo kuti akaŵagwirenso a Isirayeli anali ndani?
-Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Satana ankafuna kuti aŵagwirenso a Isirayeli?
-Satana ankafuna kuti aŵawononge a Isirayeli.

-Kodi a Isirayeli anachita chiyani atamuwona Farawo ndi asilikali ake akubwera kudzaŵagwiranso?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:10a ndi 11-12

10-Tsopano Farawo atayandikira, A Isirayeli aja adaŵawona a Ejipito akuŵalondola , ndipo adachita mantha kwambiri.

11-Adamufunsa Mose kuti, 'Kodi mchifukwa chakuti ku Ejipito kunalibe malo a manda, kuti inuyo mutifikitse ku chipululu kuno kuti tidzafe? Mwatichitira chiyani potitulutsa ku Ejipito?

12-Kodi ife tisanachoke ku Ejipito, sitinakuwuzirenitu za zimenezi? Ife tidanena kuti, "Mutileke, tikhalebe akapolo a a Ejipito." Zidakatikomela ife kukhalabe akapolo a Ejipito kupambana kuti tifere ku chipululu kuno."



-A Isirayeli ankamunena Mose kuti bolani anakatsalirabe ku Ejipito.

-Ngakhale kuti a Isirayeli anayiwona milili khumi yimene Mulungu anayitumiza mu dziko la Ejipito ija, sankakhulupilirabe mwa Mulungu.

-A Isirayeli sankakhulupilira mwa Mulungu koma Mose ankakhulupilira mwa Mulungu.

-Izi ndi zimene Mose analankhula kwa a Isirayeli:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 14:13-14

13-Apo Mose adaŵayankha anthuwo kuti, "Musawope! Limbani mtima ndipo mudzingowona zimene AMBUYE achite lero lino pofuna kukupulumutsani. A Ejipito amene mukuŵawona lerowo, simudzaŵawonanso.

14-AMBUYE ndi amene akumenyereni nkhondo. Inuyo simuchitapo kanthu kena kalikonse."

-Kodi a Isirayeli anakatha kudzipulumutsa okha?
-Iyayi.
-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli sanakatha kudzipulumutsa okha?

-Nyanja yofiira inali kutsogolo kwawo, mapili anali ku mbali zonse za iwo, ndipo Farawo ndi asilikali ake anali kumbuyo kwawo.
-A Isirayeli anakodwa.

-Kodi yekha amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayeli anali ndani?
-Mulungu.

-Adamu ndi Hava atachotsedwa kuchokera m'munda wa Edeni, sanakathanso kuloŵa m'mundamo.